

NYA_TTB_1104_SCRIPT

Yohane : 3:17-4:1

**Mutu : Kuonetsedwa kwa chikondi mu ntchito,
ndichitsimikizo chakuti pemphero lidzamveka**

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Mateyu 11:12, pamene Ambuye Yesu akunena kuti, “Ndipo kuyambira masiku a Yohane m’batizi, kufikira tsopano lino, Ufumu wa Kumwamba uli wokangamizidwa ndipo okangamirawoaukwatula ndi mphanvu.”

Mupologalamu yapita tinali kukambirana pa 1 Yohane 3:13-17, momwe timapitiliza kuona makhalidwe awiri a munthu wokhulupirira. Ndipo lero pa 1 Yohane 3:17-4:1, tisanthula nkhani yakuonetsedwakwa chikondi muntchito kuti ndichitsimikizo chakuti pemphero lidzamveka.

17.Koma iye amene ali nacho chuma cha dziko lapansi, naona m’bale wake ali wosowa ndi kutsekereza chifundo chake pommana iye, nanga chikondi cha Mulungu chikhala mwa iye bwanji?

Yohane mundime ino akunena kuti chikondi sikungolankhulamokometsera chabe, koma kuonetsa ntchito yachikondi. Yakobo m'kalata yake 2:15-16, adanenetsa kuti, "M'bale kapena mlongoakakhalawausiwa, nichikamsowa chakudya cha tsiku lake, ndipo wina wa inu akanena nawo mukani ndi mtendere, mukapfunde ndi kukhuta; osawapatsa iwo zosowa za pathupi; kupindula kwake nchiyani?" Nkhani ikunena kuti pamene m'bale wanu akudza kwa inu ndi kunena kuti tiyeni tipemphere, koma osamthandiza, sizionetsa phindu leni-leni ayi. Koma chinthu chofunika kwambiri ndicho kuonetsa kuti chikondi chanu chikuonekeradi. Tikunena kuti chinthu choopsa kwambiri ndi chakuti anthu ambiri m'dziko lapansi adzafika pamaso pa Kristu, ndi chuma chawo chochuluka cha dziko lino lapansi, chomwe sichinagwiritsidwe ntchito kuulemererowa Kristu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndikunenetsa pano kuti ndichinthu chomkomera Mulungu kuti wokhulupirira ena akhale wosowa m'zinthu zina ndi cholinga chakuti ntchito yachifundo ndi chikondi ya mkristu idziwike bwino. Komanso ndichinthu chomkomera Mulungu kuti apereke kwa akristu ena, chuma

chadziko lapansi ndi cholinga chakuti chisomo cha Mulungu chifikire akristu osauka. Tikunenetsa kuti iwo amene alinacho chuma chokoma cha dziko lapansi, ayenera kukonda Mulungu kopambana komanso kukonda akristu anzawo kopambana, kotero kuti ayenera kukhala wokonzeka kugawira chuma chawo iwo amene ndiwosowa. Ndimau amenewa tikunena kuti chikondi ichi, kwa abale chimapezeka kuchokera ku chikondi chapa Mulungu. Tere, ndichifukwa chake Yohane akunena kuti, “Koma iye amene alinacho chuma cha dziko lapansi, naona m’bale wake ali wosowa ndi kutsekereza chifundo chake pommana iye, nanga chikondi cha Mulungu chikhala mwa iye bwanji?” Kutanthauza kuti inu simungatsimikize kuti chikondi cha Mulungu chili mwa inu ngati simuchitira chifundo abale amene akusoweka chuma chokoma chadziko lapansi.

Ndiye tikunenetsa kuti, chikondi chapa abale chiyenera kuonetsedwa m’ntchito, ndipo ngati inu munganene kuti mukonda m’bale wanu popanda kuonetsachikondichom’ntchito, ndiye kuti ndinu wokhulupirira wachinyengo.

18.Tiana, tisakonde ndi mau kapena ndi lilime, komatu ndi kuchita ndi m'choonadi.

Tsono pamene Mtumwi anafika pakuti wakula ndipo sanali kuyenda ndi kukhala nawo m'misonkhano ya mpingo, koma ndiye amene anathandiza kuti mpingo ukhazikike, iye anali kubwereza-bwerezakukumbutsa za lamulo lalikuru lomwe adalilandira kuchokera kwa Kristu mwini, pomwe malamulo ena onse amangilidwapo. Ili ndilamulo limodzi lomwe lidapanga pangano latsopano kukhala losiyana, lomwe likutsindika kuti wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake.Ili, ndiganizo lomwe 1 Petro 1:22, akunena kuti, "Popeza mwayeretsa moyo wanu pakumvera choonadi kuti mukakonde abale ndi chikondi chosanyenga, mukondane kwenikweni kuchokera kumtima." Tere ndichifukwa chake akunena kuti ife sitiyenera kunena m'mau chabe, koma kuchokera kumtima. Ichi, ndicho chikondi chomwe Yohane akunena kuti, pamene inu muonetsa chikondi kuchokera kumtima kwanu, ndiye kuti chikondi chanu ndichoona komanso cheni-cheni. Ichi, ndicho chikondi chomwe Ambuye Yesu pa Mateyu 6:3, adanena kuti, "Koma iwe popatsa mphatso zachifundo, dzanja lako

lamanzerelisadziwe chimene lachita dzanja lako lamanja.”Apa, anali kunena za chikondi chomwe chikuchokerakumtima osati kumangolankhula chabe ayi. Kutanthauza kuti ndizotheka kulankhula zina ndi milomo, koma pamene mumtima muli zinthu zina.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti ndibwino kulankhula mau okoma, achikondi ndi kupereka mau achikondimaka-makakwa anthu amene ndi wopsinjika. Koma mau amenewa sayenera kuthera pomwepo ayi, popeza ndizinthuzosathandizakungonena kuti Ambuye akudalitseni popanda kuchitapo kanthu (Yakobo 2:15).Kunena kuti ndikoyenera kukamba mau achikondi amene akuchokera kumtima ndi kuonetsa ntchito zake, za chisomo cha Mulungu.Chikondi chimenechi, chimaonekera pamene abale atumikirana ndi kunyamuliranazothodwetsa, kukhululukirana ndi kupemphererana wina ndi mnzake.Ichi, ndichikondi chomwe chimachokakumtima ndipo chimaonetsedwa pakuchita ntchito mokondwera ndi mopanda mangawa, koma osati kumangonena mau odalitsa ndi achinyengo ayi.

19.Umo tidzazindikira kuti tiri ochokera m'choonadi, ndipo tidzakhazikitsa mtima wathu pamaso pake.

Nkhani ili mundime ino, ikuti pamene moyo wathu ufika poonetsa zinthu zomwe Yohane walankhulazi, tidzakhala ndi chitsimikizo chonse pamene tipempha kwa Atate. Taonani Yohane akunena kuti ndizotheka kudzachita manyazi pamene Ambuye Yesu abweranso. Iye akunena kuti anthu ambiri amalankhula zakubweransokwa Ambuye Yesu kachiwiri, koma zimaonetsa kuti sakukonzekera za kubwera kwakeko. Tikunena kuti inu ndi ine, tidzakhumudwa pamene tidzafika pamaso pa Ambuye Yesu chifukwa adzatifunsa chipatso cha moyo wathu wachikristu. Tere, ndichifukwa chake Ambuye Yesu pa Yohane 14:15, adanena kuti, “Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga.” Ndiye tikunena kuti limodzi mwa malamulo akristu likuti inu ndi ine, tiyenera kufalitsa Uthenga Wabwino, kufikira kumalekezeroadziko.Tere, funso likuti, kodi inu mukuchita china chilichonse chokhutsana ndi kufalitsa mau a Mulungu? Kapena tifunse kuti, kodi inu muli kutanganidwa ndi china chake chomwe chikusonyeza kuti ndinu mwana wa Mulungu?

Taonani kale anthu anali kuthandizana kwambiri pamene wina alikubvutika ndi matenda kapena usiwa. Ichi, ndichinthu chomwe sichikuchitika masiku ano. Mwanjira ina m' bale wake wamunthu lero lino ndi ndalama zake basi. Ngati inu mulibe ndalama musayembekeze kuti anthu ena abwera kukutengeranikuchipatala ayi. Kutsimikiza kuti anthu ambiri masiku ano, sakuchitazinthu zomwe Ambuye Yesu alinazo ndi chidwi. Koma tiyenera kudziwa kuti tsiku likubwera pomwe inu mukayankha nokha pamaso pa Kristu.

Tere, Mtumwi Yohane akulimbikitsa kuti inu ndi ine, ngati wokhulupirira sityenera kumangolankhula za chikondi pamene ife moyo wathu sukuonetsa ntchito zachikondi. Ndiye akunenetsa kuti pamene ife tichita ntchito zachikondi, ndiye kuti ndife akristu achoonadi, kotero kuti chimenechi chidzakhala chitsimikizo cha chipulumutso chathu pamaso pa Mulungu. Tsono Uthenga ukuti, kaya ndinu wosauka kaya wolemera, kutenga nawo mbalipakufalitsa mau a Mulungu chimapereka chitsimikizo mumtima kuti muli kuchita chifuniro cha Mulungu ndipo kuti mukuchita chomwe Iye afuna. Tere ndichifukwa chake Paulo

m'kalata 2 Timoteo 4:8, adanena molimbika mtima kuti, "Chotsalirawandiikira ine korona wa chilungamo, amene Ambuye, woweruza wolungama adzandipatsa ine tsiku lijalo: ndipo si kwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ake." Apa ndipo pamene Paulo anaonetsa kuti anali ndichitsimikizo chonse cha kulungama kwake. Kodi inu mudafikapotsimikiza mtima kotere?

20.M'mene monse mtima wathu utitsutsa; chifukwa Mulungu ali wamkuru woposa mitima yathu, nazindikira zonse.

Mtumwi Yohane mundime ino akunena kuti mwana wa Mulungu akhoza kukhala ndi chitsimikizo cha chipulumutso chake. Ndiye akupitiliza kuti ngakhale pakhale mwayi kwa ife wokhulupirira kuti pakhoza kukhala chitsimikizo cha chipulumutso chathu, koma akunena kuti mtima wathu ndiwo umene umatiweruza. Kutanthauza kuti mtima uli ndimphamvuzakuweruza, kotero kuti tikhoza kudziona momwe ubale wathu uli, ndi Mulungu.Mphamvu ya mtimawu, imakhozakukukuchitirani umboni, kukuweruzani ndi kukhala oweruza.Kunena kuti mtima wanu ukhoza kukuweruzani kuti simunachite bwino, kapena kukulungamitsani, kunena kuti

mwachita bwino.Mphamvu iyi, ndiyomwe inakhazikitsidwa ndi Mulungu mwa inu komanso ine.Mphamvu imeneyi, ndiyo imagwira ntchito ya nyali yomwe imaunika mkati mwathu ndi kufufuza zina zonse zobisika. Ili, ndilo ganizo lomwe likupezeka pa Miyambo 20:27, pamene pali mau akuti, “Mzimu wamunthu ndiwo nyali ya Yehova; usanthula mkati monse mwa mimba.”Tsono Uthenga ukuti mtima wanu ndiwo umene umakuweruzani inu, koma ngati mtima wanu ukuweruzani, muyenera kudziwa kuti Mulungu ndiye oweruza woposa mtima wanu popeza ndiye amadziwa zinthu zochuluka zomwe ziri mkati mwathu.Ndiye popeza Mulungu ndiye Wamkulu koposa mtima wathu, zikutsimikizadi kuti chilango chake ndi chokhazikika pa anthu onse ochimwa.Tsono nkhani ikuti ngakhale chikumbumtima chanu chikhozakukulungamitsani, koma oweruza wolungama ndiye Mulungu,ichi ndichimene akunena Paulo pa 1 Akorinto 4:4, pamene akuti, “Pakuti sindidziwa kanthu kakundiparamulitsa; koma m’menemo sindiyesedwa wolungama; koma wondiweruza ine ndiye Ambuye.”Kutsimikiza kuti mau awa ndi wolimbikitsa kuti ngati mtima wathu ungatitsutse, tiyenera kudziwa kuti Mulungu adzatiweruzanso popeza ndiye amadziwa koposa chikumbumtima chathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti kutsutsidwakwa mumtima wathu sikuti kumangochitikapaokha, koma chimakhala chochokera kwa Mulungu, amene ndi Wamkulu komanso amene adziwa zonse. Kutsimikiza kuti zonena zathu zonyenga zoturuka pakamwa pathu ndi mau othyasikasizisoweka mumtima mwathu, nanga kuli bwanji ndi Mulungu amene amadziwa zonse?Kutsimikiza kuti Mulungu ndiye Wamkulu koposa mtima wanga umene umanditsutsa, kotero kuti amadziwa chikondi changa ndi mtima wofuna kumutumikira Iye.

21.Okondedwa, mtima wathu ukapandakutitsutsa, tiri nako kulimbika mtima mwa Mulungu.

Mtumwi Yohane akunena kuti ngati chikumbumtima chathu sichikutitsutsa, ndiye kuti tikhala ndi chikhulupiriro ndi chiyembekezo chakuti pemphero lathu lidzamveka. Tikunena kuti ngati ifesitikukhaham'moyo wochita tchimo m'tseri; ngati tichita mokhulupirika zinthu zomwe ziri m'chifuniro cha Mulungu; komanso ngati tichita mopanda kunyinyilika kapena kudandaulazinthu zonse zomwe Mulungu anatipatsa kuti tiyenera kuchita. Kutanthauza kuti ngati tichita mokhulupirika ndi

motsimikiza mtima ndikutichikumbumtima chathu sichititsutsa, tikhala ndi chitsimikizo ndi chiyembekezo chonse chakuti Mulungu adzayankha pemphero lathu.

Koma tiyenera kudziwa kuti Yohane sakunena kuti munthu aliyense amene mtima wake sukumutsutsa ndiye amene alibwino pamaso pa Mulungu ayi, popeza alipo ena amene anaphachikumbumtima chawo komanso ena sadziwa choonadi. Koma tikunena kuti ngati inu mukutsimikiza mtima pachoonadi, ichi, ndichomwe chingakupulumutseni inu. Kutsindika kunena kuti akristu oona ndiwo amene adziwa malamulo akristu, kotero kuti amagwiritsa ntchito malamulo amenewa podziyesa nawo iwo eni.

22.Ndipo chimene chiri chonse tipempha, talandira kwa Iye, chifukwa tisunga malamulo ake, ndipo tichita zomkondweretsa pamaso pake.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti chikondi chomwe chimaonetsedwamuntchito, chimapereka chitsimikizo pakupemphera. Tikunena kuti pamene moyo wanu uyendamokondweretsa Mulungu, inu muyenera kuyembekeza kuti

pemphero lanu lidzamveka ndi kuyankhidwa ndithu.Mtima uwu, ndiwo umene uli wofunika kwambiri lero lino. Ndifuna mukumbukire mpingo woyamba uja, pamene kuzunzika kunayambika pakati pa wophunzira, iwoanachenjezedwa kuti asapitilize kulalikira m'dzina la Yesu. Tsono pamene wophunzira awa, ananena chimenechi kwa akristu ena, tikuona kuti mpingo wonse unalowamkupemphera. Iwowa, sadapemphere kuti kuzunzakokuthe, koma anayamba kupempheramokwezakulambira Mulungu kuti, “Mfumu, Inu ndinu wolengathambo la Kumwamba ndi dziko ndi Nyanja ndi zonse ziri m'menemo” (Mac. 4:24). Mwanjira ina akristu awa analibe nkhawa ndi kuzunzako, kotero kuti anaika chikhulupiriro chawo chonse mwa Mulungu, popeza ndiye ali ndi ulamuliro padzikolo. Ichi, ndichifukwa chake Yohane akunena kuti, ifetimalandira kwa Iye popeza tisunga malamulo ake. Kodi inu, muli nacho chikhulupiriro chotere pa Mulungu?

1 Yohane 4

Tsopano talowa m'mundimeyosautsa chifukwa chakuti tikusanthula za Mzimu, amene sitimdziwa kwenikweni.Chifukwa chachiwiri ndi chakuti inu ndi ine, tiri m'dziko la m'dierekezi kotero

kuti muli zinthu zambiri zosokoneza.Koma chinthu chofunika kwambiri ndicho kudziwa chomwe Baibuloliphunzitsa.

1. Okondedwa, musakhulupiriremzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati ikuchokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi.

Mtumwi Yohane akuyamba ndi mau achikondi ndi cholinga chakuti akristu atchere khutu popeza akuyamba kulankhula nkhani yofunika kwambiri.Taonani akuyamba ndi kuchenjeza kuti akristu sayenera kukhulupirira aliyense amene anena kuti ndiwodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ichi, ndichimene Ambuye Yesu pa Mateyu 24:4, adachenjezeratu kuti, “Yang’aniranasasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzafika m’dzina langa, nadzanena, Ine ndine Kristu, nadzasokeretsa anthu ambiri.” Tikunena kuti atumiki oona ndi onama, onse amanena kuti akutumikira ndi Mzimu wa Mulungu, kotero kuti ndikofunika kuti Mzimu uliwonse uyese dwe. Kunena kuti akristu oyamba aja samayenera kungolandira aliyense amene akunena kuti watumidwa kuchoka kwa Mulungu ayi. Iwo, amayenera kupeza umboni wonse kuti anali wochokeradikwa Mulungu, popeza panali atumiki ambiri onyenga. Kutanthauza

kuti anthu onse amene amanena kutindiwochokerakwa Mulungu, amayenera kuyesedwa mokwanira chifukwa cha kuchuluka kwa anthu amene amadzitcha kuti ndiwo wochokera kwa Mulungu.

Tsono mumpingo woyamba uja munali akristu ena amene anali ndi nzeru yosiyanita mizimu. Izi, sizikutanthauza kuti akristuwa anali ndimphamvuyapadera ayi, koma kuti aliyense amayenera kusiyanita ziphunzitso ndi zikhulupiriro zawo ndi zomwe zikupezeka m' mau a Mulungu. Komanso akristuwa amayenera kuona zipatso za chikhulupiriro chawo m'moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Kunena kuti akristu amayenera kuona ngati atumikiwa amaphunzitsa zomwe mau a Mulungu anena ndi kuona ngati moyo wawo ukugwirizana ndi zomwe amaphunzitsazo. Komanso amaonetsetsa ngati moyo waaphunzitsiwo unali kugwirizana ndi zomwe zimayenerakutsatidwa ndizomwe iwo anaphunzitsidwa poyamba ndi aphunzitsi oona. Ichi, ndichimene 1 Yohane 4:6, akunena kuti, "Ife ndife ochokera mwa Mulungu; iye amene azindikira Mulungu atimvera; iye wosachokera mwa Mulungu satimvera ife. Momwemo tizindikira Mzimu wa choonadi, ndi Mzimu wa chisokeretso." Kutsimikiza kuti atumiki awa amayenera

kuwalandira monga momwe anali, kapena kuwakana kuti ndiwo atumiki onama.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ine ndikuona kuti tsopano nthawi yafika yakumayesa ziphunzitso zonse kuti tione ngati zikuchokeradikwa Mulungu. Tikunena kuti inu mukhoza kuzindikira atumiki oona pamene ziphunzitso zawo zikuchokera m' mau a Mulungu. Mwachimenechi, ndikosatheka kungozindikira kuti ichi, ndichiphunzitso choona pokhapokha inu mukhale ndi mtima wosanthula mau a Mulungu. Ichi, ndichimene akristu aku Berea anali kuchita, nthawi zonse akamva mau a Mulungu, amakhalanso ndi nthawi nasonkhana pamodzi ndi kuyamba kusanthula ngati mauwo ali oona kapena ayi.

Ndifuna kutsiriza ndi mau akuti, Yohane adaona kuti aphunzitsi ambiri amene amadzitchakuti ndiatumiki oona, anali kuphunzitsa zoipa kotero kuti unali udindo wawo kuonetsetsa kuti ziphunzitso zoipazozisalowe mumpingo wawo. Kodi inu mukuteteza motani ziphunzitso zoipa zilipolerozi?

Lero tilekeza pano. Ndipo timasanthula 1 Yohane 3:17-4:1, momwe timakambirana nkhani yakuonetsedwakwa chikondi muntchito kuti ndichitsimikizo chakuti pemphero lidzamveka.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!